# KUBZALA MITENGO NDI KUSAMALILA

## Malangizo a alimi ang'ono-ang'ono a m'magulu

## Kodi kubzala mitengo n'kutani?

Iyi ndi dongosolo yochotsa tumitengo tung'ono-tung'ono tofesedwa (mbande) pa nasale kapena tosonyeza/chitsanzo kukabzala pamalo achikhalile.

## Kodi ulimi wa mbewu ndi mitengo n'chiyani?

Ulimi wa mbewu ndi mitengo ndi njila yaulimi imene alimi amasunga mitengo ndi zitsamba limodzi n'mbewu zina kapena n'zinyama pamalo amodzi kuchilikiza ulimi wabwino.

## Ndi mapindu ati alipo pa ulimi wa mbewu ndi mitengo?

- Mitengo imatipatsa mpweya wopuma ndi madzi akumwa.
- Mitengo imatipatsa chakudya, chakudya cha ziweto, nkhuni, mathunthu/milando, matabwa/mapulanga, mankhwala, ndi zina zotelo.
- Mitengo ina imaika mpweya wa nitrogen mu nthaka kuti mbewu zizidya.
- Mitengo ina imathandizila nthaka kutenga/kunyowa ndi kusunga madzi.
- Mitengo imachilikiza kapangidwe kanthaka n'kuthandizila kuchepetsa kukokoloka kwa nthaka ndi chimphepo.
- Mitengo imatipatsa kudzidzila ndi mthunzi.

Promotion of agroforestry

Supported by:

unique land use

With support from

Federal Ministry of Food and Agriculture

by decision of the German Bundestag

Prepared by: Daniel M. Kalala; Graphic design: Jonathan Leya

# Ndondomeko yotsatila pobzala mbewu ndi mitengo m'munda




**Kunyamula mbande/tomela kupeleka ku munda –** musapeputse nthawi ndi kuyesetsa kwanu kofunikila kunyamula tumitengo kukabzala pamalo anu mwakonza. Munganyamule mbande m'matadza, pa njinga, ngolo, galimoto kapena ndi thalakita. Njila mudzasankha kunyamulila idzadalila maka-maka pa mtunda kumene mudzabzala ndi kuchuluka kwa tumitengo. Sewenzetsani ngolo ngati tumitengo n'twambili (300 kapena kuposapo). Ganizilani galimoto kapena thalakita ngati mbande zili zoposa 1,000.




**Kandandalikidwe ka munda –** Ganizilani malo osiyana pobzala mitengo yamitundu-mitundu: Bzalani mitengo iika feteleza m'nthaka (Gliricidia) pafupi n'mbewu zanu. Ija mitengo ifuna chisamalilo chachikulu mubzale m'dimba kapena pafupi ndi nyumba kuti muiteteze bwino masiku onse.










**Kukonzekela dzenje ndi kubzala mitengo –** Kumbani dzenje lalikulu bwino kuti mizu yonse ilowe ndipo ikani dothi mosiyana, nthaka ya pamwamba kumbali imodzi kumbali kwinaku katondo (4); Ikani nthaka yosakaniza ndi manyowa, Bokashi kapena manyowa owolela m'dzenje mukalibe kubzalamo kamtengo (5A). Chotsani kamtengo m'pulasitiki ndi kuika m'dzenje (5B). Onetsetsani kuti kamtengo mukubzala poyambila mizu yake pali chabe pamwamba pa dothi (6A). Bwezelani dothi yapamwamba/nthaka-manyowa/zowolela/Bokashi ndi dothi ina ya katondo m'mbali mwa kamtengo (6B) ndi kuthilila.

# Kutalikilana kwa mitundu-mitundu ya mitengo yobzalidwa m'munda

6

| Tree species | Spacing (m) | | Planting hole L×W×D (cm) |
|---|---|---|---|
| | Pakati pa mizele | Motalika | |
| Gliricidia (alley cropping) | 5 | 1 | 30×30×40 |
| Manga | 7 | 7 | 60×60×60 |
| Malalanje okwatitsa pa ndimu | 5 | 5 | 60×60×60 |
| Papaya | 5 | 5 | 60×60×60 |
| Moringa | 3 | 2 | 30×30×40 |
| Khaya (Mubaba) | 3 | 3 | 30×30×40 |
| Leucaena | 3 | 1 | 30×30×40 |
| Kubzala mbewu osafesa | | | |
| Tephrosia (alley cropping) | 5 | 1 | Ikani mbewu m'dzenje mmene mumabzalila chimanga. |
| Pigeon pea (alley cropping) | 5 | 1 | |
| Tephrosia (mbewu kapena kupangila biomass) | 1 | 1 | |
| Pigeon pea (mbewu kapena zakudya za ziweto) | 1 | 1 | |

**Kutalikana –** Mitengo yosiyana-siyana imafuna madanga osiyana malinga ndi:

(I) *Maonekedwe a mtengo* - mitengo ya thunthu/kolona yaikulu/ yotakata imafuna kutalikilana kwambili kuposa ya thunthu ing'ono.

(ii) *Kulolela kwa mitundu ya mitengo* - mpata ung'ono ku mitengo ikonda mthunzi ndi kutalikana mitengo ifuna dzuwa.

(iii) *Mtundu wa mbewu ndi mitengo idzabzalidwa* - osatalikitsa mpata wa mitengo kapena zitsamba zolimidwa kamodzi kutengako mbewu, zakudya za ziweto kapena biomass(zowolela), kenako kutalikitsa mpata wa mitengo/zitsamba zosewenzetsa mu ulimi wa mpata ndi mbewu (alley cropping system.




**Kutalikana kwa mitengo ya feteleza yobzalidwa mu ulimi wa mbewu ndi mpata** - mpata ung'ono pa mitengo monga gliricidia ndi leucaena kuti ipange biomass (zowolela/chonde) yambili kuthandizila kupangachonde. Kugwetsa mayani kawili-kawili kwa mitengoyi pokula kumachepetsa mpikitsano pakati pa mitengo ndi mbewu ndipo imabweza biomass/ zowolela/chondo mu nthaka.




**Kutalikilana kwa mitengo yazipatso** - mipata ikulu kwambili imapelekedwa maka-maka ku mitengo yazipatso kuchepetsa kulimbana zakudya komanso kuonetsetsa kuti mitengo ikubala zipatso zochuluka ndi zabwino kwambili.

**Kutalikana kwa mitengo kapena zitsamba zobzalidwa mosafesa** - mpata ung'ono umasiidwa pa mitengo monga Tephrosia ndi pigeon peas chifukwa mwina simungadziwe kuti mbewu zingamele bwino. Pambuyo pomela, kuzulamo mbewu zina kungachitike kusiyamo zofunika.

**Kutalikana kuti mulime mitengo ya matabwa kapena nkhuni** - mipata ikulu imasiidwa pa mitengo monga Mubaba imene imalimidwa kupangila matabwa/mapulanga kuonetsetsa kuti mtengo ukulandila zakudya bwino kuti ukapange mapulanga abwino. Mitundu yamitengo yankhuni nthawi zambili imakula mwamsanga ndipo mpata ung'ono ndiwoyenelela chifukwa mitundu imeneyi izidulidwa kawili-kawili kutengako nkhuni.